



HELMINTHS

CHINSINSI CHA MOYO WA NYONGOLOTSI ZOYAMBISA MATENDA



wellcome
centre
integrative
parasitology



CHINSINSI CHA MOYO WA NYOGOLOTSI ZOYAMBITSA MATENDA NDI BUKU LA NTHABWALA LOMWE LINASINDIKIZIDWA NDI WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY, A JAMIE HALL NDI A EDWARD ROSS MUCHAKA CHA 2020.

BUKULI LINALEMEDWA NDI A JAMIE HALL NDI A EDWARD ROSS. LINANTHAUZIRIDWA MUZINTHUNZI NDI A EDWARD ROSS. DR. POPPY LAMBERTON NDI DR. RICK MAIZELS ANATHANDIZA NDI ULANGIZI WA SAYANSI.

ULAMULIRO WONSE WA BUKU LI NDI WA WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY NDI OLEMBA. SIKOLOLEDWA KUTI GAWO LILILONSE LA BUKULI LITSINDIKIZIDWE KAPENA KUKOPEDWA MWANJIRA ILIYONSE POPANDA CHILOLEZO CHA OTSINDIKIZA NDI OLEMBA.

BUKULI LINASINDIKIZIDWA NDI A WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY, SIR GRAEME DAVIES BUILDING, UNIVERSITY OF GLASGOW, 120 UNIVERSITY PLACE, GLASGOW, G12 8TA.

ILI NDI TANTHAUZIRIDWE LA BUKULI MU CHICHEWA.


BUKULI LINA SINDIKIZIDWA PA MAPEPALA OBWEZEREDWANSO

TSIKU LINANSO LABWINO M'MBALI
MWA NYANJA YA VICTORIA





ZIKUONEKA NGATI CHINACHAKE
CHABISALA M'MADZIMU




MPHUTSI ZOYAMBITSA
MATENDA A LIKODZO


NYONGOLOTSI ZOKHALA NGATI
TIZILOMBO TOYAMBITSA MATENDA
KUFUNAFUNA THUPI LA MUNTHU
KUTI TILOWEMO



MONGA MWA
CHONCHO


WATITENGA
TIZILOMBO






TAFIKA MU NTHAWI YAKE! LERO TIKHALA
TIKUPEREKA MANKHWALA A MATENDA A
LIKODZO KWA MUDZI ONSE

KOMA NDE MALO
OONEKA BWINO!




KUNO NDIKWABWINO
KWAMBIRI KOMA VUTO
LALIKULU TILI NALO NDI
MATENDA WA.

MATENDA WA AMAYAMBITSIDWA NDI
TIZILOMBO TA MTUNDU WA NYONGOLOTSI TOMWE
TIMAKHALA MU NKHONO ZA M'MADZI
TISANAPHULIKE NDIKULOWA M'THUPI LA MUNTHU




KU SCOTLAND,
TIMANGOGANIZIRAKO ZA NKHONO
ZIKAKHALA KUTI ZIKUONONGA
MASAMBA M'DIMBA.

MULI NDI MWAYI, NKHONO
KWATHU KUNO ZIMAFALITSA MATENDA
KOMANSO ZIMADWALITSA ANTHU.



ANTHU OKWANA 200 MILIYONI
DZIKO LONSE LAPANSI, AMAPEZEKA
NDI TIZILOMBO TOYAMBITSA LIKODZO,
AMBIRI MWA IWO NDIOCHOKERA KU
MWERA KWA SAHARA, KU AFRICA

MU MATAWUNI NDI MIDZI YA
M'MBALI MWA NYANJA KUNOKO,
PAFUFUPI ALIYENSE ANAKHALAPO
NDI TIZILOMBO TI PA NTHAWI
INA YAKE.



UYU NDI NAMAZZI, NTHAWI
ZONSE NDIMAMULANGIZA ZA
KUIPA KOSAMBIRA M'NYANJA
KOMA SAMAMVA.

KOMATU MWANA ALIYENSE KUNO
AMASAMBIRA M'NYANJA. NDE
MUKUONA NGATI NDIZIKAZIRITSA
KUTIKO NDIKATENTHEDWA?

NDASANGALALA KUKUMANA
NAWE NAMAZZI. NDACHOKERA KU
SCOTLAND, NDABWERA KUDZAMUONA
MOSES KUTI NNDIZIWE ZAMBIRI ZA
NTCHITO IMENE AKUGWIRA.

PANO UKUPEZA
BWANJI NAMAZZI?

PANG'ONO, NDAKHALA
NDISAKUPITA KU SUKULU
CHIFUKWA CHODWALA.

TIMAMUTCHA
BAMBO WA NKHONO

KWA ANA NGATI NAMAZZI, LIKODZO
LIMAYAMBITSA KUTSEGULA NDI KUPWETEKWA
M'MIMBA. IZI, ZIMAPANGITSA ANA KUJOMBA
KU SUKULU KOMANSO ANA WA AMAKHALA
OTOPA KOMANSO ODWALA

KWA NTHAWI YAITALI, MAZIRA
A NYONGOLOSI ZOYAMBITSA
MATENDAWA, AMAMANGANA
M'THUPI ZOMWE ZIMAKHALA
ZOOPSA KWAMBIRI

KOMA IZIZI
SIZINGAKUCHITIKILE IWEYO
NAMAZZI CHIFUKWA
UPATSIDWA THANDIZO
KOMANSO UKHALA KUTALI
NDI MADZI, SICHONCHO?

IZI
NDIZOONA
MOSES.

TIMALANDILA MAPIRITSI AWULERE OCHOKELA
KU BUNGWE LA WORLD HEALTH ORGANISATION, NDIPO
NDIKOSAVUTA KUWAPATSA ANTHU CHITHANDIZO
KUSIYANA NDIKUWAYEZA KAYE NGATI ALI
NDILIKODZO KAPENA AYI

CHAKA CHATHA,
TINAKWANITSA
KUTHANDIZA
ANTHU PAFUPIFUPI
MAZANAMAZANA
AWIRI.

KOMA PALI VUTO LOMWE TIKUKUMANA
NALO, CHIWERENGERO CHA ANTHU ODWALA
LIKODZO CHIKUMAKHALA CHOKWERA NTHAWI
ZONSE TIKABWERANSO. IZI ZIKUSONYEZA
KUTI ANTHU AKUMATENGABE LIKODZO

NAMAZZI, UYU NDI POPPY. AKUTSOGOLERA GULU LOCHOKERA KU WELCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY AMENE ALI PAKAFUKUFUKU WOPEZA NJIRA YOTHETSERA KUFALA KWA LIKODZO

HI!

NDASANGALALA TAKUMANA

EKO! TASONKHANITSA ZIYEZO ZA CHIMBUDZI KUTI ZI YEZEDWE!

KOMA ABALE!

ZIYEZO ZA CHIMBUDZI?

MAZILA OYAMBITSA MATENDAWA AMATULUKA M'THUPI KUZERA M'CHIMBUDZI. UMU NDI MMENE TIZILOMBO TI TIMAPEZEKA TABWELELA M'MADZI NDI NKHONO

POYANG'ANA MAZILA A TIZILOMBO TI MU CHIMBUDZI, TIMATHA KUDZIWA AMENE ALI NDI MATENDA WA KOMANSO TIMATHA KUUNIKA MAJINI A TIZILOMBO TOBISIKATI.

NDAZILEMBETSERA NTCHITO YANJI KODI?

TIYENI TIYAMBEPO KUSEFA.

NDI CHITHUNZITHUNZI CHAMA JINI, TIMATHA KUDZIWA MMENE TIZILOMBO TI TIMAGWILIRA NTCHITO KOMANSO MMENE TIMAFANANIRANA. CHIFUKWA CHA IZI, TIKHOZA KUPHUNZIRA ZAMBIRI

NDIKUONANSO CHONCHOTU.


TIZILOMBO TOYAMBITSA LIKODZO





VUTO LINA NDILOKUTI PENNA MANKHWALA WA SAMAGWIRA NTCHITO.

SAMAGWILA?



KUTI MAPIRITSI AGWIRE NTCHITO, AMAYENERA ADUTSE M'MATUMBO MWATHU, NDIKULOWA M'MAGAZI MOMWE TIZILOMBO TI TIMABISALA



CHOTI TIDIWE NDIHOTI ALIYENSE WA IFE ALI NDI MA JINI OSIYANASIYANA KOMANSO TIZILOMBO TOSIYANASIYANA TOMWE TIMAKHALA M'MATUMBO MWATHU.

PALI ANTHU ENA MATUMBO AWO AMAYAMWA MANKHWALA ONSE PAMENE ENA PANG'ONO CHABE.

ZIMATENGELANSO ZOMWE WADYA KUMENE.




NDIYE TIZILOMBO TI TIMAKUMANA NDI MLINGO YOSIYANASIYANA YA MANKHWALA KUTENGERA NDI AMENE WAPEZEKA NAKO KACHILOMBOKA?

EYA, NDIPO NGATI MLINGO SUNAKWANE, TIMAPATSA MWAYI TIZILOMBO TI KUTI TISINTHE NDI NDIKUKHALA OSAPHEDWA NDI MANKHWALA.




ICHI NDICHIFUKWA CHAKE TIKUZUKUTA MA JINI A TIZILOMBO TI.




TIKAFANANIZA MMENE MATENDAWA AKULOWERA M'THUPI MOSIYANASIYANA, TIKHOZA KUDZIWA MMENE TIZILOMBO TI TIMAFALIKIRA KOMANSO KUSINTHIKA



OSADANDAULA JANE, LERO TILI PANTCHITO YOTI TIPEZE NJIRA ZOYEZERA TIZILOMBO TI POTENGA MIKODZO. NDIZOSADANDAUITSA KWAMBIRI NGATI CHIMBUDZI.




NGAKHALE TITAPEZA MWAYI
WOPEZA NDI KUTHANA NDI MATENDA
WA MWA ANTHU, NYANJA ZATHU
ZIKANALI ZODZADZA NDI NKHONO
ZOMWE ZILI NDI TIZILIMBO TAMBIRI
TOYAMBITSA LIKODZO



ANTHU AMBIRI AMAKHALA MAOLA
AMBIRI ALI M'MADZI AKUCHAPA ZOVALA
NDI KUWEDZA NSOMBA, KUMENE
KUMAONJEZERETSA MWAYI WOPEZKA
NAWO MATENDA WA

NDIPO NTHAWI ZINA, ZOIPA
ZOCHOKERA KUCHIMBUDZI,
ZIMATHANSO KULOWA M'NYANJA.
UMU NDI MMNENE TIZILIMBO TI
TIMAPEZEKA TACHOKA M'THUPI LA
MUNTHU NKUBWERELANSO
NDIKUKALOWA MU NKHONO,
NKUYAMBILANSO NDONDOMEKO
YONSE MMENE MATENDAWA
AMAYAMBIRA.



NDIYE, TIKUNGOYENERA KUKHALA A LUSO.
SITIMANGOLEMBA AKATSIWIRI AZA SAYANSI
OKHA AYI, KOMANSO TIMALEMBA AKATSIWIRI
OONA ZA CHUMA NDI AKATSIWIRI
AZACHIKHALIDWE KOMANSO AZISUDZO


AZISUDZO?




TAPEZA AZISUDZO OMWE AZITHANDIZIRA KUFALITSA
UTHENGA WA KAPEWEDWE KA MATENDAWA

INDEI,
OSACHITA
CHIMBUDZI
M'NYAJA

TIKUYESETSA KUWAFIKILA ANTHU AMENE AMAKANA CHITHANDIZO
POWAONETSA MMENE KACHILOMBOKA KAMAFALITSIKIRA



AKATSIWIRI AZACHIKHALIDWE AMATITHANDIZA KUMVETSA
ZISANKHO ZOMWE ANTHU AMAPANGA. MWA CHITSANZO, ANTHU
AMADALIRA MADZI OMWEWO PA MOYO WAWO WA TSIKU NDI TSIKU



PANO, TIMAWALETSA ANTHU KUCHAPA ZOVALA ZAWO
ALI CHIYIMIRIRE MMADZI. TSPANO, AMACHAPIRA PA
MTUNDA, ZOMWE ZIMATHANDIZA KUCHEPETA
KUTENGA TIZILIMBO TOYAMBITSA LIKODZO TU



ZOONA ZAKE NDIZAKUTI, UMPHAWI UMATENGA GAWO LALIKULU PA MATENDA WA. MADERA AMENE ALI OSAUKA AMAKUMANA NDI MAVUTO OCHULUKA OKHUDZA UKHONDO AMENE AMAPANGITSA MATENDA KUCHULUKA. PAMENEPA NDIPAMENE AZACHUMA AKU GLASGOW AMABWERAPO.


AMAGWIRA NTCHITO NDI ANTHU AMU MIDZI KUTI APEZE NJIRA ZODALILIKA, ZODZIWIKA KOMANSO ZOSABOOLA NTHUMBA KUTI ABWELETSE ZIMBUDZI KOMANSO MADZI AUKHONDO MU MADELA MWAWO.



POPEZA NJIRA ZOKHAZIKIKA ZOPITITSA PATSOGOLO UKHONDO, TITHA KUKWANITSA KUPEWA CHIMBUDZI KAPENA MIKODZO KULOWA M'NYANJA KOMANSO KULIMBANA NDI NJIRA ZOMWE MATENDAWA AMAYAMBIRA NDI KUFALIKIRA.



KOMA NDE ZABWINOTU KWA ANTHU OSAMBILAFE




UM, OSAMBILA AKALE



NANGA NKHONO ZI, NDI CHANI CHOMWE TINGAPANGE KUTI TITHANE NAZO?

NDIKUONA NGATI KUZIPONYA MU DIMBA LA NEBA SIZINGAKHALE BWINO?



NTHAWI ZINA, TIMAGWIRITSA NTCHITO MANKHWALA POFUNA KUPHA NKHONOZI, KOMA SITINGAKWANITSE KUZIPHA ZONSE KOMANSO ZILI NDI KUFUNIKIRA KU CHILENGEDWE

INETU NDINKAGANIZA KUTI TITHANE NDI MATENDA WA, TIKUYENERA KUKHALA NDI MANKWALA OYENELERA, KOMA NDAONA KUTI NDI ZOVUTIRAPO.

NGATI TIKUFUNA KUSINTHA MIYOYO YA ANTHU, TIKUYENERA TIPHATIKIZE NJIRA ZODALILIKA ZONSE, KUSINTHA CHIKHALIDWE CHATHU NDI KUKHALA A UKHONDO

KOMANSO KUTHANA NATO NDI TIZILOMBO TI POKUPHA TIZILOMBO TONSE.

KUTIPHA TONSE? OSAKHALA NDI PHUMA

NAMAZZI, UYU NDI RICK, KATAKWE PA NKHANI ZA NYONGOLOTSI!

NDIZOONA, TIZILOMBO TOONEKA NGATI NYONGOLOTSI TI NDITOOPSA. TIZILOMBO TI, TAKHALA TILI PAKATI PATHU CHILENGELENI DZIKO LAPANSI.

KUYAMBILA NTHAWI IMENYO, TAKHALA TIKUSINTHA MODABWITSA POFUNA KUKHALABE NDI MOYO M'MATUPI ATHU

PALI TIZILOMBO TAMBIRI TOONEKA NGATI NYONGOLOSI. TINA MWA TIZILOMBO TI TILI NDIKUTHEKERA KOSOKONEZA CHITETEZO CHATHU CHA M'THUPI, CHIMENE CHIMATHANDIZIRA KULIMBANA NDI TIZILOMBO TOSAFUNIKA M'THUPI!

NDIYEZ?

NDE MWINATU TIZILOMBO TI TIKHOZA KUTIPHUNZITSA ZINTHU ZINGAPO

MATENDA AMBIRI MONGA MPHUMO, ZIWENGO NDI MITUNDU INA YA NYAMAKAZI ZIMAYAMBA PAMENE CHITETEZO CHATHU CHA M'THUPI CHASOKONEKERA POLIMBANA NDI ZINTHU ZOMWE ZILIBE VUTO M'THUPI MWATHU

KUKHALA NDI TIZILOMBO TOONEKA NGATI NYONGOLITSI TI KULI NDI KUTHEKERA KOTHETSA ENA MWA MATENDA A CHITETEZO CHA M'THUPI WA. NDIPO, KAFUKUFUKU ALI MKATI PAKALI PANO MOTI ENA MWA ODWALA MATENDAWA AKUMABAYIDWA NYONGOLITSI KUTI ACHIRE

EW.

EYETU, NGAKHALE ZIKUTHANDIZA, KUDWALA CHIFUKWA CHA NYONGOLITSI ZI SIKWABWINO. NDIYE TIKUMACHITA IZI NDI CHOLINGA CHOTI TIDZIWE MMENE NYONGOLITSIZI ZIMASOKONEZELA CHITETEZO CHATHU CHA M'THUPI KUTI ZIKHALE NDI MOYO


NYONGOLITSI ZINA ZIMALAVULA MALOVU OMWE ALI NDIKUTHEKERA KOONEKA NGATI MBALI INA YA CHITETEZO CHATHU CHA M'THUPI, PAMAPETO PAKE NKUCHEPETA CHITETEZO AKHOZA. KAPENA MWINA MALOVU WA AKHOZA KUGWIRITSIDWA POCHEPETA MATENDA ENA A ZA CHITETEZO MONGA MPHUMO

ZIMAKOPELA CHITETEZO CHATHU CHA M'THUPI, TSOPANO NANU MUFUNA MUZIKOPELE?


UMM, NDALIMBIKITSIDWA. KULIMBIKITSIDWA NDI NYONGOLITSI ZIKUMVEKA NGATI NTHABWALA

KUSINTHA KWA NYONGOLITSI KUTI ZI ZIKHALA BWINO NDI ANTHUFE KUNGATHENSO KUPEKA MWAYI OZIGONJETERA KAPENA KUGONJETA MATENDA ENA. MMENE NDIANENERA MU, ZIDA ZINA ZIMENE TINGAGWIRITSE NTCHITO ZIMACHOKERA M'MALO ODABWITSA NDITHU.


NDENDENDE!



SINDIMADZIWA KUTI ANTHU ALI KALIKILIKI KUGWIRA NTCHITO MOLIMBIKA KUTI INE NDI ANZANGA TIZIKHALA BWINO, TISAMADWALEDWALE.




TIZILOMBO TOKHALA NGATI NYONGOLOTSI TI TIMAPANGITSA ANTHU KUTI AZIVUTIKA, AMAPEZEKA SAKUPITA KUNTCHITO KOMANSO KU SUKULU NDIPONSO TIMAYAMBITSA MAVUTO AMGONAMGONA PA MOYO WAWO.




TILI NDI CHIKHULUPIIRO KUTI TSIKU LINA MATENDAWA TIDZAKWANITSA KUWAGONJETSA



MWINA MKATI MWA NDIMEMU, TIKHOZA KUPINDULA POPEZA NDIKUGWIRITSA NTCHITO ZINSINSI ZINA ZA TIZILOMBO TI



MWINA INE NKHUKHALA OTETEZEKA POKASAMBILA KOMANSO A BAMBO ANGA POKAWEDZA NSOMBA



TSIKU LINA. PANOPA UZDIKUMBUKILA KUTI ULI NDI ANTHU NGATI MOSES, POPPY NDI RICK OCHOKELA KU KAMPALA MPAKA KU GLASGOW OMWE ALI PAKALIKILIKI KUGWIRA NTCHITO MOLIMBIKA KUTI ATHANE NAWO MATENDAWA



wellcome
centre
integrative
parasitology



WELLCOME CENTER FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY IMAPEZEKELA KU
SUKULU YA UKACHENJEDWE YA GLASGOW. NTCHITO YATHU YAIKULU NDI
KUFUFUZA ZA MMENE TIZILOMBO TOYAMBITSA MATENDA
OSIYANASIYANA TIMAGWILRA NTCHITO M'THUPI MWA MUNTHU KUTI
TIPEZE MANKHWALA NDI NJIRA ZOTIGONJETSERA

KUTI MUDZIWE ZAMBIRI ZA NTCHITO YATHU, ONANI TSAMBA LA INTANETI
GLA.AC.UK//RESEARCHINSTITUTES/III/WCIP

KAPENA CHEZANI NAFE PA TSAMBA LA MCHEZO LA TWITTER
[@WCIPGLASGOW](https://twitter.com/WCIPGLASGOW)

TIKUTHOKOZA DR POPPY, DR RICK. DR VICKIE NDI ONSE AMENE ANATENGAPO GAWO
POWELENGA BUKULI KUTI LIMVEKE BWINO


ZAMBIRI ZA OLEMBA BUKU LA NTHABWALI MUZNGAZIPEZE PA

WWW.EDWARDROSS.CO.UK

WWW.JPJHALL.NET

KHALANI NAWONI A KATSWIRI AZASAYANSI OCHOKERA KU GLASGOW
PAMENE ALI PA ULENDU WOPITA KU UGANDA KUKAFUFUZA ZA CHINSINSI
CHA NYONGOLOTSI ZOYAMBITSA MATENDA NDI KUDWALADWALA KWA
ANTHU PADZIKO LONSE LAPANSI

MBALI IMODZI YA NKHANI ZA TIZIROMBO IMENE INAWINA MPHOTO



**wellcome
centre
integrative
parasitology**

